

||

***AKHRISTU
NDI
KUWERUZA***

Kodi akhristu angathe kuweruza?

||

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

||

***AKHRISTU
NDI
KUWERUZA***

Kodi akhristu angathe kuweruza?

||

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

AKHRISTU NDI KUWERUZA

Kodi akhristu angathe kuweruza? Nkhani yakuweruza ndiyovuta ngakhale buku lopatulika likufotokozera bwino za kuweruza. Pa **Mateyu 7v1-5**, Yesu akuti tisaweruze. Kuyang'anitsitsa mawuwa, Yesu akukamba za kuweruza kwa pamunthu kapena kwa chinyengo, kutifotokozera kuti tiyambe tachotsa chitsotso chomwe chiri mu diso lathu (**v5**). Komanso ndizachidziwikire kuti tisaweruze maganizo kapena malingaliro amunthu wina, pakuti sitidziwa chomwe iwo ali, (**1 Akorinto 2v11**). Pa **Yohane 7v14**, pokhudza za lamulo, Yesu akuti: *“musaweruze monga maonekedwe, koma weruzani chiweruzilo cholungama”* Mwachimvekere tikupemphedwa kuweruza zokhudza chikhulupiliro komanso moyo wa chilungamo. (**Mateyu 7v15** komanso **Aroma 16v17**). Tikalephera kutsatira pempho ili, ndiye kuti buku lopatulika lidzangokhala ngati buku lina liri lonse ndipo ife tidzakhala opanda maziko. Tidzakhala ngati ana a Israeli mu nthawi ya oweruza: *“Panalibe mfumu mu Israyeli masiku aja yense anachita chomkomera pamaso pake.”* (**Oweruza 21v25**)

AKHRISTU NDI KUWERUZA

Kodi akhristu angathe kuweruza? Nkhani yakuweruza ndiyovuta ngakhale buku lopatulika likufotokozera bwino za kuweruza. Pa **Mateyu 7v1-5**, Yesu akuti tisaweruze. Kuyang'anitsitsa mawuwa, Yesu akukamba za kuweruza kwa pamunthu kapena kwa chinyengo, kutifotokozera kuti tiyambe tachotsa chitsotso chomwe chiri mu diso lathu (**v5**). Komanso ndizachidziwikire kuti tisaweruze maganizo kapena malingaliro amunthu wina, pakuti sitidziwa chomwe iwo ali, (**1 Akorinto 2v11**). Pa **Yohane 7v14**, pokhudza za lamulo, Yesu akuti: *“musaweruze monga maonekedwe, koma weruzani chiweruzilo cholungama”* Mwachimvekere tikupemphedwa kuweruza zokhudza chikhulupiliro komanso moyo wa chilungamo. (**Mateyu 7v15** komanso **Aroma 16v17**). Tikalephera kutsatira pempho ili, ndiye kuti buku lopatulika lidzangokhala ngati buku lina liri lonse ndipo ife tidzakhala opanda maziko. Tidzakhala ngati ana a Israeli mu nthawi ya oweruza: *“Panalibe mfumu mu Israyeli masiku aja yense anachita chomkomera pamaso pake.”* (**Oweruza 21v25**)

kuweruza mwachilungamo ndikulekelera, popeza zidzapangitsa munthu wochimwa kupita ku chionongeko. Ndipo izi zingapangitse mipingo yochita chilungamo kukhala ngati mabungwe basi.

Mulungu akuitanira anthu ake kukupatuka ndi kuchiyero, osanyengerera.

Khalani mlonda, mmalo mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by Mick Alexander
Email: leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

kuweruza mwachilungamo ndikulekelera, popeza zidzapangitsa munthu wochimwa kupita ku chionongeko. Ndipo izi zingapangitse mipingo yochita chilungamo kukhala ngati mabungwe basi.

Mulungu akuitanira anthu ake kukupatuka ndi kuchiyero, osanyengerera.

Khalani mlonda, mmalo mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by Mick Alexander
Email: leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

Nafenso tiyenera kudzudzula tchimo pamene tatsimikizika. Chilungamo ndichakuti tikulamulidwa kutsutsa tchimo. **1 Timoteo 1v3-5** akuti “...ukalamulire ena ajawa asaphunzitse kanthu kena ... koma chitsiriziro cha chilamulo ndicho chikondi chochokera mu mtima woyera ndi chikumbumtima chokoma ndi chikhulupiliro chosanyenga.”

Bungwe lokakamiza umodzi mu chikristu likunamiza ambiri achipembedzo ku umodzi wa chiyembekezo chabodza omwe sulankhula zakulapa ndi kukhulupilira Ambuye Yesu Khristu. Anthu ochuluka akutsatira chiphunzitsochi. Yesu akuti: “Iye wosakhala pamodzi ndi Ine akana Ine, ndi iye wosasonkhanitsa pamodzi ndi Ine, amwazamwaza.”. **Mateyu 12v30.**

Kodi mutalakwitsa, simungafune wina akubwezeni mbuyo? Ngati mungatero, nanunso, mwachikondi, mumbweze mbale wanu yemwe akusokera. **Yakobo 4v17** akutichenjeza kuti: “Potero kwa iye amene adziwa kuchita bwino ndipo sachita, kwa iye kuli tchimo.” Kulephera

Nafenso tiyenera kudzudzula tchimo pamene tatsimikizika. Chilungamo ndichakuti tikulamulidwa kutsutsa tchimo. **1 Timoteo 1v3-5** akuti “...ukalamulire ena ajawa asaphunzitse kanthu kena ... koma chitsiriziro cha chilamulo ndicho chikondi chochokera mu mtima woyera ndi chikumbumtima chokoma ndi chikhulupiliro chosanyenga.”

Bungwe lokakamiza umodzi mu chikristu likunamiza ambiri achipembedzo ku umodzi wa chiyembekezo chabodza omwe sulankhula zakulapa ndi kukhulupilira Ambuye Yesu Khristu. Anthu ochuluka akutsatira chiphunzitsochi. Yesu akuti: “Iye wosakhala pamodzi ndi Ine akana Ine, ndi iye wosasonkhanitsa pamodzi ndi Ine, amwazamwaza.”. **Mateyu 12v30.**

Kodi mutalakwitsa, simungafune wina akubwezeni mbuyo? Ngati mungatero, nanunso, mwachikondi, mumbweze mbale wanu yemwe akusokera. **Yakobo 4v17** akutichenjeza kuti: “Potero kwa iye amene adziwa kuchita bwino ndipo sachita, kwa iye kuli tchimo.” Kulephera

Tikati titsatire malamulo a Mulungu monga: “...musayanjane naye ngati wina wotchedwa mbale ali wachigololo, kapena wosilira, kapena wopembedza mafano, kapena wolalatra, kapena woledzera, kapena wolanda, kungakhale kukadya naye wotere, iai. Pakuti nditani nawo akunja kukaweruza iwo? Kodi amene ali m’katimo simumawaweruza ndi inu; koma akunja awaweruza Mulungu? Chotsani woipayo pakati pa inu nokha.” **1 Akorinto 5v11-13**

“Yesani zonse, sungani chokomacho.”

1 Atesalonika 5v21

“... dana nacho choipa, gwirizana nacho chabwino.” **Aroma 12v9**

“... yang’anirani iwo akuchita zopatutsana ndi zopunthwitsa, kosalingana ndi chiphunzitso munachiphunzira inu. Ndipo potolokani pa iwo.”

Aroma 16v17

Tsono funso lisakhale “Kodi tingaweruze?” koma likhale “Ndi zinthu ziti zomwe tingaweruze?”

Aroma 14 ndi zotsutsana za makani

Aroma 14 akufotokozerana zinthu zomwe sitikuyenera kuweruza popeza ndi zotsutsana za makani (**v1**) Zotsutsana za makani ndi zinthu kapena zochitika zomwe sizipindulira ku

Tikati titsatire malamulo a Mulungu monga:

“...musayanjane naye ngati wina wotchedwa mbale ali wachigololo, kapena wosilira, kapena wopembedza mafano, kapena wolalatra, kapena woledzera, kapena wolanda, kungakhale kukadya naye wotere, iai. Pakuti nditani nawo akunja kukaweruza iwo? Kodi amene ali m’katimo simumawaweruza ndi inu; koma akunja awaweruza Mulungu? Chotsani woipayo pakati pa inu nokha.” **1 Akorinto 5v11-13**

“Yesani zonse, sungani chokomacho.”

1 Atesalonika 5v21

“... dana nacho choipa, gwirizana nacho chabwino.” **Aroma 12v9**

“... yang’anirani iwo akuchita zopatutsana ndi zopunthwitsa, kosalingana ndi chiphunzitso munachiphunzira inu. Ndipo potolokani pa iwo.”

Aroma 16v17

Tsono funso lisakhale “Kodi tingaweruze?” koma likhale “Ndi zinthu ziti zomwe tingaweruze?”

Aroma 14 ndi zotsutsana za makani

Aroma 14 akufotokozerana zinthu zomwe sitikuyenera kuweruza popeza ndi zotsutsana za makani (**v1**) Zotsutsana za makani ndi zinthu kapena zochitika zomwe sizipindulira ku

chipulumutso komanso Mulungu sanazifotokozere mwakuya. Pokhala zotsutsana, munthu amakhala ndi ufulu osankha monga zakudya (v2), tsiku lopatulika (v5). Zovala zikhoza kukhala zotsutsana koma zikuyenera kukhala zaulemu komanso zoyenera (1 **Timoteo 2v9**). Zokhudza tsitsi zafotokozeredwa pa **1 Akorinto 11v14-15**.

Zikhoza kukhala zovuta kudziwa malire a kavalidwe kapena kuti tsitsi likhale lotalika bwanji koma v21 ikofotokozera bwino pamene mawu akuti: *“kuli kwabwino kusadya nyama, kapena kusamwa vinyo, kapena kusachita chinthu chiri chonse chakukhumudwitsa m’bale wako.”* Komanso **1 Akorinto 10v31-32** akuti: *“chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonse kuulemelero wa Mulungu. Khalani osakhumudwitsa kapena Ayuda kapena Ahelene, kapena Mpingo wa Mulungu.”* Ma vesiwa akufotokozera momveka kuti ngati tikhumudwitsa m’bale wathu ndi zomwe tikuchita, tikuyenera kusiya kuchita chinthu chimenecho. Kwaife zikhoza kukhala zosakhumudwitsa, koma kwa wina zikhoza

chipulumutso komanso Mulungu sanazifotokozere mwakuya. Pokhala zotsutsana, munthu amakhala ndi ufulu osankha monga zakudya (v2), tsiku lopatulika (v5). Zovala zikhoza kukhala zotsutsana koma zikuyenera kukhala zaulemu komanso zoyenera (1 **Timoteo 2v9**). Zokhudza tsitsi zafotokozeredwa pa **1 Akorinto 11v14-15**.

Zikhoza kukhala zovuta kudziwa malire a kavalidwe kapena kuti tsitsi likhale lotalika bwanji koma v21 ikofotokozera bwino pamene mawu akuti: *“kuli kwabwino kusadya nyama, kapena kusamwa vinyo, kapena kusachita chinthu chiri chonse chakukhumudwitsa m’bale wako.”* Komanso **1 Akorinto 10v31-32** akuti: *“chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonse kuulemelero wa Mulungu. Khalani osakhumudwitsa kapena Ayuda kapena Ahelene, kapena Mpingo wa Mulungu.”* Ma vesiwa akufotokozera momveka kuti ngati tikhumudwitsa m’bale wathu ndi zomwe tikuchita, tikuyenera kusiya kuchita chinthu chimenecho. Kwaife zikhoza kukhala zosakhumudwitsa, koma kwa wina zikhoza

Ndizolakwika kusadzudzula choipa pamene zikudziwikiratu kuti miyoyo ikupita kuchionongeko. Amanena kuti “tisaweruze, tikhale mu umodzi,” ndipo pakutero miyoyo ikupita ku gehena tsiku ndi tsiku. Yesu akutiwuzwa momveka pa **Mateyu 24** kuti padzadzuka aneneri onyenga ndipo ife tisamale kuti tisanyengedwe. Tikuyenera kudzudzula chinyengo poyera:

a) Paulo anawatchula anthu ochita chinyengo pa **2 Timoteo 2v16-17, 2 Timoteo 4v14-15**, komanso **1 Timoteo 1v19-20**.

b) Yohane anamutchula munthu pa **3 Yohane 1v9-10**.

c) Paulo anadzudzula poyera m’tumwi mzake pa **Agalatiya 2v11, 14**.

d) Atsogoleri ochita chinyengo akuyenera kudzudzulidwa poyera monga mawu akunenera pa **1 Timoteo 5v20**.

e) A khristu ochita tchimo mosaleka akuyenera kudzudzulidwa pamaso pa mpingo monga mawu akunenera pa **Mateyu 18v15-17**

f) Mu mawu ena monga **2 Akorinto 11v5, 13v15**, komanso **Chibvumbulutso 2v2**, ochita zolakwikawo sanatchulidwe koma wolandira makalatawo anali kudziwa anthu omwe anali kuchita zachinyengowo.

Ndizolakwika kusadzudzula choipa pamene zikudziwikiratu kuti miyoyo ikupita kuchionongeko. Amanena kuti “tisaweruze, tikhale mu umodzi,” ndipo pakutero miyoyo ikupita ku gehena tsiku ndi tsiku. Yesu akutiwuzwa momveka pa **Mateyu 24** kuti padzadzuka aneneri onyenga ndipo ife tisamale kuti tisanyengedwe. Tikuyenera kudzudzula chinyengo poyera:

a) Paulo anawatchula anthu ochita chinyengo pa **2 Timoteo 2v16-17, 2 Timoteo 4v14-15**, komanso **1 Timoteo 1v19-20**.

b) Yohane anamutchula munthu pa **3 Yohane 1v9-10**.

c) Paulo anadzudzula poyera m’tumwi mzake pa **Agalatiya 2v11, 14**.

d) Atsogoleri ochita chinyengo akuyenera kudzudzulidwa poyera monga mawu akunenera pa **1 Timoteo 5v20**.

e) A khristu ochita tchimo mosaleka akuyenera kudzudzulidwa pamaso pa mpingo monga mawu akunenera pa **Mateyu 18v15-17**

f) Mu mawu ena monga **2 Akorinto 11v5, 13v15**, komanso **Chibvumbulutso 2v2**, ochita zolakwikawo sanatchulidwe koma wolandira makalatawo anali kudziwa anthu omwe anali kuchita zachinyengowo.

Tikayang'ana mwakuya; pa dziko lonse lapansi pali ma tchalichi, anthu olalikira pa kanema, komanso aphunzitsi a uthenga wabodza ndi machiritso onama, komanso uthenga wolemera (wolanda chuma) monga mawu akunenera pa **2 Petro 2**. Mawu a Mulungu akutipempha kupatukana ndi izi: *".....koma iwe munthu wa Mulungu iwe, thawa izi: nutsate chilungamo, chipembedzo, chikhulupiriro, chikondi, chipiliro, chifatso.... Dana nacho choipa gwirizana nacho chabwino kapena kuunika."* (**1 Timoteo 6v11; Aroma 12v9; ndi 2 Akorinto 6v14**) Mulungu akutsutsana ndi uthenga onyenga pa **Agalatiya 1v8** *"Koma ngakhale ife kapena mngelo wochokera kumwamba, ngati akulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa."* Zomwe Mulungu akutsutsana nazo, ifenso tikuyenera kuchenjeza anzathu kuti angakodwe, ndipo nawonso angadzaweruzidwe. **1 Akorinto 2v15** akuti: *"Koma iye amene ali wa uzimu, ayesa zonse"* ndipo **1 Yohane 4v1** akutiuzanso kuti *"...yeseni mizimu.."* Khalani ngati m'Beleya ndikusiyantsa ziphunzitsa zonse ndi mawu a Mulungu, osati kukhulupilira zinthu zomwe ndi zotchuka.

Tikayang'ana mwakuya; pa dziko lonse lapansi pali ma tchalichi, anthu olalikira pa kanema, komanso aphunzitsi a uthenga wabodza ndi machiritso onama, komanso uthenga wolemera (wolanda chuma) monga mawu akunenera pa **2 Petro 2**. Mawu a Mulungu akutipempha kupatukana ndi izi: *".....koma iwe munthu wa Mulungu iwe, thawa izi: nutsate chilungamo, chipembedzo, chikhulupiriro, chikondi, chipiliro, chifatso.... Dana nacho choipa gwirizana nacho chabwino kapena kuunika."* (**1 Timoteo 6v11; Aroma 12v9; ndi 2 Akorinto 6v14**) Mulungu akutsutsana ndi uthenga onyenga pa **Agalatiya 1v8** *"Koma ngakhale ife kapena mngelo wochokera kumwamba, ngati akulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa."* Zomwe Mulungu akutsutsana nazo, ifenso tikuyenera kuchenjeza anzathu kuti angakodwe, ndipo nawonso angadzaweruzidwe. **1 Akorinto 2v15** akuti: *"Koma iye amene ali wa uzimu, ayesa zonse"* ndipo **1 Yohane 4v1** akutiuzanso kuti *"...yeseni mizimu.."* Khalani ngati m'Beleya ndikusiyantsa ziphunzitsa zonse ndi mawu a Mulungu, osati kukhulupilira zinthu zomwe ndi zotchuka.

kumukhumudwitsa komanso kuononga chikhulupiliro chawo. (**1 Akorinto 8v1-13; 10v23-33 makamaka v31-3**). **1 Akorinto 9v22** Paulo akuti: *"kwa ofoka ndinakhala ngati ofoka kuti ndipindule ofoka. Ndakhala zonse kwa anthu onse, kuti pali ponse ndikapulumutse ena."* Kuchokera pa vesili, tikuona kuti tiyenera kusamala ndi machitidwe athu kwa anthu osapulumsidwa chifukwa tikhoza kukhala mboni zolakwikwa kwa iwo.

Choncho, ngakhale zinthu zomwe zili zopanda pake, tikuyenera kuweruza mosamala kuti tisagwetse munthu wina. Izi sizingasokoneze chikhulupiliro cha munthu chokha ayi, komanso **Aroma 14v10-12** akutichenjeza kuti wina aliyense waife adzaweruzidwa malingana ndi ntchito zake pamaso pa Mulungu. Tikuchenjezedwanso pa **Yakobo 4v11-12** kuti kunenerana kapena kuweruzana kufanana ndi kuweruza lamulo la Mulungu lomwe likutilamula kukondana ndi m'bale wathu. **Aroma 13v8** akuti: *"..pakuti iye amene akondana ndi mzake wakwanitsa lamulo."*

kumukhumudwitsa komanso kuononga chikhulupiliro chawo. (**1 Akorinto 8v1-13; 10v23-33 makamaka v31-3**). **1 Akorinto 9v22** Paulo akuti: *"kwa ofoka ndinakhala ngati ofoka kuti ndipindule ofoka. Ndakhala zonse kwa anthu onse, kuti pali ponse ndikapulumutse ena."* Kuchokera pa vesili, tikuona kuti tiyenera kusamala ndi machitidwe athu kwa anthu osapulumsidwa chifukwa tikhoza kukhala mboni zolakwikwa kwa iwo.

Choncho, ngakhale zinthu zomwe zili zopanda pake, tikuyenera kuweruza mosamala kuti tisagwetse munthu wina. Izi sizingasokoneze chikhulupiliro cha munthu chokha ayi, komanso **Aroma 14v10-12** akutichenjeza kuti wina aliyense waife adzaweruzidwa malingana ndi ntchito zake pamaso pa Mulungu. Tikuchenjezedwanso pa **Yakobo 4v11-12** kuti kunenerana kapena kuweruzana kufanana ndi kuweruza lamulo la Mulungu lomwe likutilamula kukondana ndi m'bale wathu. **Aroma 13v8** akuti: *"..pakuti iye amene akondana ndi mzake wakwanitsa lamulo."*

Khalani a Beleya ndi kusanthula malemba – Act 17v11

Komabe, sizonse zomwe zili za makani otsutsana. Kuti mukazindikire kuti chinthu chiri cha makani otsutsana; muzifunse nokha funso ili:- ‘Kodi chinthu ichi chingasokoneze chipulumutso cha munthu wina?’ Ngati yankho ndi inde, mungatsimikizike kuti Mulungu akutichenjeza nacho ndipo ifenso titelo. Ichi ndi chinthu chofunika kwambiri ndipo chiri ndi mfundo ziwiri. Munthu akhoza kusocheretsedwa osati chifukwa cha zonedwa kapena kuchitika kokha ayi, komanso chifukwa cha zosanenedwa kapena zosachitika. Chipulumutso cha moyo ndi chaphindu lamuyaya ndipo tikuyenera kusamalitsa ndi zomwe tikuchita komanso zomwe sitichita. Tonse tikudziwa zotsatira za kuchita zoipa. Komanso Mulungu akutichenjeza kuti kusachita bwino kuli ndi zotsatira zake. Pa **Ezekiel 33v1-9** Mulungu akuchenjeza wolondera kuti akalephera kuomba lipenga, ndikuchenjeza anthu, mlondayo adzaweruzidwa mlandu. M’khristu wina aliyense ndi mlonda.

Khalani a Beleya ndi kusanthula malemba – Act 17v11

Komabe, sizonse zomwe zili za makani otsutsana. Kuti mukazindikire kuti chinthu chiri cha makani otsutsana; muzifunse nokha funso ili:- ‘Kodi chinthu ichi chingasokoneze chipulumutso cha munthu wina?’ Ngati yankho ndi inde, mungatsimikizike kuti Mulungu akutichenjeza nacho ndipo ifenso titelo. Ichi ndi chinthu chofunika kwambiri ndipo chiri ndi mfundo ziwiri. Munthu akhoza kusocheretsedwa osati chifukwa cha zonedwa kapena kuchitika kokha ayi, komanso chifukwa cha zosanenedwa kapena zosachitika. Chipulumutso cha moyo ndi chaphindu lamuyaya ndipo tikuyenera kusamalitsa ndi zomwe tikuchita komanso zomwe sitichita. Tonse tikudziwa zotsatira za kuchita zoipa. Komanso Mulungu akutichenjeza kuti kusachita bwino kuli ndi zotsatira zake. Pa **Ezekiel 33v1-9** Mulungu akuchenjeza wolondera kuti akalephera kuomba lipenga, ndikuchenjeza anthu, mlondayo adzaweruzidwa mlandu. M’khristu wina aliyense ndi mlonda.

Tikulamulidwa kuweruza m’bale wathu pokhudza moyo wao. Akorinto anauzidwa kuti:”....*chotsani woipayo pakati pa inu nokhakuti lionongeke thupi, kuti mzimu apulumutsidwe m’tsiku la Ambuye Yesu.*” **1 Akorinto 5v13, 5.** Munthu uyu anachotsedwa pakati pawo, koma poyambilira anaweruzidwa ngati wochimwa ndi abale ake mwa Khristu.

Kuonjezera apo, **Yakobo 5v19-20** akuti: “....*Abale anga, ngati wina wa inu asochera posiyana ndi choonadi, ndipo ambweza iye mzache; azindikire kuti iye amene abweza wochimwa ku njira yake yosochera adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvindikira machimo aunyinji.*” Sikotheka kutsatira malangizo awa tisanaweruze. Zikhoza kukhala zovuta kutero, koma ndichikondi chomwe chingatikakamize kufikira ndi kuweruza osochera; ndipo ngati sititero, tikhala opanda udindo. Ngati sitikwanitsa kukhala moyo wa chiyero, mpingo udzakhala opanda chiyero, ndipo padzangokhala ngati pa malo osonkhana ndikuchita zomwe aliyense akuona ngati ndizoyenera.

Tikulamulidwa kuweruza m’bale wathu pokhudza moyo wao. Akorinto anauzidwa kuti:”....*chotsani woipayo pakati pa inu nokhakuti lionongeke thupi, kuti mzimu apulumutsidwe m’tsiku la Ambuye Yesu.*” **1 Akorinto 5v13, 5.** Munthu uyu anachotsedwa pakati pawo, koma poyambilira anaweruzidwa ngati wochimwa ndi abale ake mwa Khristu.

Kuonjezera apo, **Yakobo 5v19-20** akuti: “....*Abale anga, ngati wina wa inu asochera posiyana ndi choonadi, ndipo ambweza iye mzache; azindikire kuti iye amene abweza wochimwa ku njira yake yosochera adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvindikira machimo aunyinji.*” Sikotheka kutsatira malangizo awa tisanaweruze. Zikhoza kukhala zovuta kutero, koma ndichikondi chomwe chingatikakamize kufikira ndi kuweruza osochera; ndipo ngati sititero, tikhala opanda udindo. Ngati sitikwanitsa kukhala moyo wa chiyero, mpingo udzakhala opanda chiyero, ndipo padzangokhala ngati pa malo osonkhana ndikuchita zomwe aliyense akuona ngati ndizoyenera.